-NthaŵI zonse Mulungu amapereka chilango pa tchimo lililonse ndi imfa yosatha.

-Ngati mumaŵakonda machimo anu ngati mkazi wake wa Loti, Mulungu adzakulangani inu ndi imfa.

-Ngati simukufuna kuŵasiya machimo anu ngati mkazi wake wa Loti, Mulungu adzakulangani inu ndi imfa.



## PHUNZIRO LA 21

1. Kodi vuto limene linalipo pakati pa Loti ndi Abulamu linali lotani?
-Chifukwa chakuti Abulamu ndi Loti anali ndi nkhosa ndi ng'ombe zambiri, kunalibe msipu okwanira woti mkumadyetsera ziweto zawo zonse.

2. Kodi chifukwa chiyani Loti anasankha kukakhala ku chigwa?
-Chifukwa chakuti kunali msipu wambiri wodyetsera ziweto zake.

3. Kodi chifukwa chiyani Loti anapanga chisamkho choyipa chokakhala ku chigwa?
-Chifukwa chakuti Loti sanamufunse Mulungu chimene anakachita.
-Chifukwa chakuti loti anakana kumumvera Mulungu.

4. Kodi chidzakuchitikirani chiyani tikamakana kumumvera Mulungu?
-Tikamakana kumumvera Mulungu, tidzapita ku Nyanja ya Moto Wosatha.

5. Kodi chuma chanu chidzakupulumutsani inu ku Nyanja ya Moto wosatha?
-Iyayi.

6. Kodi Mulungu amkakuwona kuchimwa kwa anthu a ku Sodomu ndi Gomora?
-Inde.

7. Kodi tingabise china chilichonse chimene tikuganiza kwa Mulungu?
-Iyayi.

8. Kodi tingabise china chilichose chimene timalankhula kwa Mulungu?
-Iyayi.

9. Kodi tingabise china chilichonse chimene timachita kwa Mulungu?
-Iyayi

10. Kodi Mulungu anamuwuza chiyani Abulamu, Loti atapita ku chigwa?
-Mulungu ananena kuti adzamupatsa Abulamu dziko lonse la kanani.
-Mulungu ananenanso kuti Abulamu adzakhala ndi zidzukulu zochuluka ngati nyenyezi.
-Mulungu analankhulanso kuti zidzukulu za Abulamu zidzapita kukakhala ku dziko lina, koma pakadzatha zaka 400, Mulungu adzadzibwerezanso ku Kanani.

11. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamupatsa Abulamu ndi Sarayi mayina atsopano?
-Chifukwa chakuti adzakhala ndi zidzukulu zambiri.

12. Kodi dzina latsopano limene Mulungu anamupatsa Abulamu linali ndani?
-Abulahamu.

13. Kodi dzina latsopano limene Mulungu anamupatsa Sarayi linali ndani?
-Sara.

14. Kodi chifukwa chiyani Abulahamu ndi Sara analibe ana?
-Sara anali osabereka.
-Abulahamu pamodzi ndi Sara anali okalamba kwambiri.

15. Kodi Abulahamu ndi Sara anali ndi zaka zingati?
-Abulahamu anali ndi zaka 100 ndipo Sara anali ndi zaka



-Mulungu amapereka chilango pa machimo onse.
-Mulungu amapereka chilango pa machimo onse ndi imfa yosatha.

-Mu nthaŵI ya Nowa, Mulungu anaŵawononga anthu onse ndi chigumula cha madzi.
-M'mizinda ya Sodomu ndi Gomora, Mulungu anaŵawononga anthu onse ndi moto.

-Pamene angelo aja anamutenga Loti, mkazi wake ndi ana ake akazi aŵiri aja, naŵatulutsira kunja kwa mzinda wa Sodomu, anamuwuza Loti ndi banja lake kuti asachewukire kumbuyo.

-Koma mkazi wa Loti sanamvere.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 19:26

26-Koma mkazi wa Loti anachewukira kumbuyo,
ndiye pomwepo anasanduka mwala wa mchere.

-Mulungu anamusandutsa mwala wa mchere mkazi wa Loti.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamusandutsa mkazi wa Loti mwala wa mchere?
-Chifukwa chakuti mkazi wa Loti sanamumvere Mulungu, ndipo anachewukira m'mbuyo.

-Kodi chifukwa chiyani mkazi wa Loti anachewukira m'buyo?
-Chifukwa chake amkaŵakonda machimo ake.
-Chifukwa chakuti samkafuna kuti aŵasiye machimo ake.

-Mulungu amalida tchimo.
-NthaŵI zonse Mulungu amapereka chilango pa tchimo lina lililonse.

-Mulungu sanamupulumutse Loti chifukwa chakuti anali wabwino.

-Ngakhale kuti Loti sanali ngati anthu a mu mzinda wa Sodomu uja, Loti anabadwa ali ochimwa.
-Loti anabadwiranso mu tchimo ngati anthu ena onse.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu anamupulumutsa Loti?
-Chifukwa chakuti Loti amkadziwa kuti anamuchimwira Mulungu.
-Chifukwa chakuti Loti amkadziwa kuti tchimo lake lidzamubweretsera imfa yosatha.

-Chifukwa chakuti Loti amkadziwa kuti Mulungu yekha ndi amene angathe kumupulumutsa iye.
-Chifukwa chakuti Loti amkakhulupilira kuti Mulungu adzatumiza Mpulumutsi kudzamupulumutsa iye.

-Nthaŵl zonse Mulungu amaŵapulumutsa anthu amene amakhulupilira mwa Iye.

-Kodi chinachitika ndi chiyani Mulungu atamutulutsa Loti ndi banja lake mu mzinda wa Sodomu?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 19:24-25

24-Kenako AMBUYE anagwetsa moto wa sulufule pa Sodomu ndi Gomora kuchokera kumwamba.
25-Chomcho anayiwonongeratu mizinda imeneyi, pamodzi ndi chigwa chonse ndi anthu onse a m'mizindamo, kuphatikizanso zomera zonse za m'dziko limenelo.

-Mulungu anaŵawonongeratu anthu onse a m'mizinda ya Sodomu ndi Gomora.

-Mulungu amadana ndi tchimo.





16. Kodi amene analenga munthu wamamuna ndi munthu wamkazi woyamba anali ndani?
-Mulungu yekha.

17. Kodi pali chinthu china chilichonse chimene sangachithe kuchichita Mulungu?
-Palibe.

-Kodi mukukumbukira kuti Abulamu ndi Loti anasiyana chifukwa chakuti aliyense mwa iwowo anali ndi nkhosa ndi ng'ombe zambiri, ndipo kunalibe msipu okwanira woti mkumadyetsera ziweto zawo zonse?

-Kodi Abulahamu anapita kukakhala kuti?
-Ku mapiri.

-Kodi Loti anapita kukakhala kuti?
-Ku chigwa.

-Kodi mayina a mizinda iŵiri imene inali ku chigwacho anali chiyani??
-Mayina a mizinda imeneyi anali Sodomu ndi Gomora.

-Kodi anthu a ku Sodomu ndi Gomora anali otani?
-Anthu a ku Sodomu ndi Gomora anali ochimwa kwambiri.

-Kodi Mulungu amkakudziŵa kuchimwa kwa anthu a ku Sodomu ndi Gomora?
-Inde.

-Kodi Mulungu amkakudziŵa bwanji kuchimwa kwa anthu a ku Sodomu ndi Gomora?
-Mulungu amaziwona zinthu zonse.
-Palibe china chilichonse chimene Mulungu sangachiwone.

-Mulungu anakuwona kuchimwa konse kwa anthu a ku Sodomu ndi Gomora.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 18:20-21

20-Kenako AMBUYE anati, “Pali zolakwa zoopsya zo-khudza Sodomu ndi Gomora, ndipo tchimo lawo ndi lalikuru kwambiri.
21-Chomcho ndikuti nditsikireko kuti ndikawone ngati zo-lakwa zimene ndamvazo ndi zowona. Ngati sichoncho ndi-dzadziŵa.”

-Mulungu amkadziŵa za kulakwa kwa anthu a ku Sodomu ndi Gomora kwa nthaŵI yayitali.

-Anthu a ku Sodomu ndi Gomora anayiwala za Mulungu, koma kodi Mulungu anayiwala za iwowo?
-Iyayi.

-Anthu a ku Sodomu ndi Gomora anayiwala za  Mulungu, koma kodi Mulungu anayiwala za tchimo lawo?
-Iyayi.

-Kodi anthu akayiwala za Mulungu, Mulungu amaŵayiwala iwowo?
-Iyayi.

-Kodi anthu akayiwala za Mulungu, Mulungu amayiwala za machimo awo?
-Iyayi.

-Mulungu sangayiwale tchimo.
-Mulungu akuyenera kupereka chilango pa tchimo lililonse.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu akuyenera kupereka chilango pa tchimo lililonse?
-Chifukwa chakuti Mulungu anaŵalenga anthu ali abwino



kotero kuti sanathenso kuliwona khomo.

12-Anthu aŵiriwo anamufunsa Loti kuti, “Kodi aliponso wina aliyense amene uli naye kuno? Tenga ana ako amuna ndi akazi, akamwini ako ndi wina aliyense wachibale amene ali mu mzinda muno, mutuluke,

13-chifukwa chakuti ife tikufuna kuti tiwononge malo ano. AMBUYE aziwona zoyipa zonse zimene anthu amene akukhala mu mzinda muno akuchita, ndipo tatumidwa kuti tiwuwononge mzindawu.”

14-Pamenepo Loti anapita kwa anyamata amene amkafuna kukwatira ana akewo nawawuza kuti, “Fulumilani, tiyeni tituluke kuno, chifukwa chakuti patsala pang’ono kuti ANBUYE awononge malo ano.” Koma iwowo amkangoyesa nthabwala chabe.

15-M’mamaŵa, angelo aja anayesa kumufulumizitsa Loti namuwuza kuti, “Fulumira! Iweyo ndi mkazi wako ndi ana ako akazi aŵiri, mutuluke kupita kunja kwa mzinda, kuti mupulumutse moyo wanu pamene mzinda uno ukuwo-nongedwa .”

16-Koma Loti amkakayikabe, koma AMBUYE ana-mumvera chifundo. Chomcho anthu aja anatenga Loti, mkazi wake ndi ana ake akazi aŵiri aja moŵagwira pa dzanja, naŵatulutsa mu mzindamo, mkuŵasiya panja pom-wepo.

17-Ataŵatulutsira kunja kwa mzindawo, m’modzi mwa angelowo anati, “Thamangani, mupulumutse moyo wanu, musachewukire m’mbuyo, ndipo musayime m’chig-wamo. Thaŵirani ku mapirikuti mungaphedwe.”

-Angelo aja anagwira manja a Loti, mkazi wake, ndi ana ake akazi aŵili aja, naŵatulutsira kunja kwa mzindawo.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamupulumutsa Loti?
-Kodi Mulungu anamupulumutsa Loti chifukwa chakuti anali wabwino?
-Iyayi.

akathyole chitseko.

-Anthu aku Sodomu ndi Gomora anali oyipa kwambiri.

-Anthuwo amkalankhula zinthu zabodza zambiri.
-Anthuwo amkaŵanamizira anthu ena zinthu zambiri.
-Anthuwo amkaŵatembelera abale awo.

-Anthuwo amkaba zinthu za anthu ena.
-Anthuwo amkagona ndi akazi a amuna ena.
-Anthuwo amkapha anthu ena.
-Anthuwo amkagonananso ndi amuna amzawo.

-Kodi anthu a masiku ano ali ngati anthu a ku Sodomu ndi Gomora?
-Inde.

-Kodi anthu a masiku ano tikufanana bwanji ndi anthu a m'mizinda ya Sodomu ndi Gomora?
-Anthu a masiku ano timanama kwambiri.
-Anthu a masiku ano takhala tikuŵanamizira anthu ena zinthu zambiri.
-Anthu a masiku ano takhala tikuŵatembelera abale athu.
-Anthu a masiku ano takhala tikuba zinthu zambiri za anthu ena.
-Anthu a masiku ano takhala tikugona ndi akazi a amuna ena.
Anthu a masiku ano takhala tikuŵapha anthu ena.

-Kodi kenako angelowo anachita chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 19:10-17

10-Koma anthu aŵiri amene anali mkati aja, anamukokera Loti mnyumba, natseka chitseko.
11-Kenako anaŵachititsa khungu anthu onse amene anayima pa bwalowo, achinyamata ndi okalamba omwe,



kwambiri.
-Chifukwa chakuti tchimo lililonse limatsutsana ndi Mulungu.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu sanangofikira kupereka chilango kwa anthu a ku Sodomu ndi Gomora chifukwa cha machimo awo?
-Chifukwa chakuti Mulungu amkafuna kuti anthu a ku Sodomu ndi Gomora alape machimo awo.
-Chifukwa chakuti Mulungu amkafuna kuti aŵapulumutse anthu a ku Sodomu ndi Gomora.

-Kodi mu nthaŵi ya Nowa, Mulungu anaŵadikilira anthu nthaŵi yayitali bwanji kuti alape machimo awo?
-Zaka 120.

-Kodi Mulungu anachita chiyani, Iye atawona kuti anthu sanalapebe machimo awo?
-Anatumiza chigumula cha madzi chimene chinawononga anthu onse.

-Mulungu amaŵadikilira anthu kuti alape machimo awo.
-Koma ngati anthu sakulapabe machimo awo, Mulungu amaŵalanga iwowo.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu sakufuna kungofikira kupereka chilango kwa anthu chifukwa cha machimo awo lero lino?
-Chifukwa chakuti Mulungu akufuna kuti anthu tilape machimo athu.
-Chifukwa chakuti Mulungu akufuna kutipulumutsa.

-Kodi Mulungu amangofuna kuwawopsyeza anthu, koma asaŵapatsa chilango chifukwa cha machimo awo?
-Iyayi.
Mulungu adzapereka chilango pa machimo onse.

-Kodi nthaŵI ikadzakwana yakuti Mulungu apereke chilango kwa nthu ochimwa, pali amene angadzathe kumuletsa Iye.
-Palibe.

-NthaŵI ikadzakwana yakuti Mulungu apereka chilango kwa anthu ochimwa, palibe amene angadzathe kuti athawe chilango cha Mulungu.

-Tsiku lina Mulungu anatumiza angelo Ake aŵiri ku Sodomu.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 19:1-3

1-Angelo aŵiri aja analowa mu Sodomu madzulo ndi kachisisira, Loti atakhala pafupi ndi chipata cha mzindawo. Tsopano Loti atangowawona anthuwo, anayimilira naŵalonjera. Anaŵeramitsa mutu, nati,
2-Chonde Ambuye anga, tiyeni mukafike ku nyumba, mukatsuke mapazi ndikugona komweko. M'mawa kukacha mungathe kupitilira ndi ulendo wanu." Koma iwo anayankha kuti, "Iyayi, ife tigona panja mu mzinda mom'muno."
3-Loti anawumulirabe kuŵapempha, ndipo pambuyo pake iwo anavomera, napita ku nyumba kwa Loti. Kenako Loti anaŵachitira phwando. Anaŵaphikira mkate osafufumitsa naŵakonzera chakudya chokoma kwambiri, anthuwo mkudya.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anatumiza angelo Ake aŵiri ku Sodomu?
-Chifukwa chakuti Mulungu amkafuna kuti ampulumutse Loti ndi banja lake.

-Poyamba, Loti amkakhala pafupi ndi mzinda wa Sodomu.
-Tsopano, Loti amkakhala mkati mwa mzinda wa Sodomu.

-Poyamba, Loti amkakhala pafupi ndi machimo a mu mzinda wa Sodomu.



-Tsopano, Loti amkakhala mkati mwa machimo a mu mzinda wa Sodomu.

-Kodi mukuwona zimene limkachita tchimo kwa Loti?
-Tchimo limkamuŵamundikitsirabe Loti ku kuyipa kwake.

-Umu ndi m'mene limachitira tchimo kwa anthu onse.
-Tchimo limaŵandikitsirabe anthu ku kuyipa kwake.

-Tchimo limaŵandikitsirabe anthu ku kulakwa kwake ngati m'mene tchimo limkamuŵandikitsirabe Loti ku Sodomu.

-Kodi chinachitika ndi chiyani kwa angelo aja atamuyendera Loti?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 19:4-9

4-Alendowo asanakagone, anthu onse a mu mzinda wa Sodomu, achinyamata ndi okalamba omwe, anadzayizungulira nyumbayo.
5-Anamuyitana Loti namufunsa kuti,"Kodi anthu amene abwera kwanu usiku uno aja ali kuti? Atulutse, abwere kuno kuti tigone nawo."
6-Loti anatuluka panja natseka chitseko
7-kenako anaŵapepha kuti. "Inu, abwenzi anga, musachite zimenezi chifukwa ndi kulakwa kwambiri kuchita zotere.
8-Onani, ine ndili ndi ana akazi aŵiri, anamwali osamudziŵa mamuna. Bwanji ndikupatseni ana amenewa kuti muchite nawo zimene mukufunazo? Koma alendowa musachite nawo kanthu kena kalikonse chifukwa ndi alendo anga, ndipo ndiyenera kuŵatchinjiriza."
9-Koma iwowo anati, "Choka apa wakudza iwe! Ndiwe ndani iwe kuti ungatiwuze zoti tichite? Tachoka apa! Mwina mwake tingathe kukuzunza kwambiri kuposa iwowo."Chomcho anamukankha Lotiyo, nasendera kuti